

KUCHOKA KU CHIKAIKO KUPITA KU CHITSIMIKIZO

من الشك إلى اليقين

Nkhani yoona ya kufuna funa choonadi.

Chichewa — التشيشيوا

Ndinali ndikukaika za kupezeka kwa mulengi, ndipo chikaiko chimenechi chinali chikundisowetsa mtundere.

Ndipo ndinali ndikuganiza kuti palibe pa dziko la pansi munthu okhulupilira. Ndithu ndinafika pa mulingo umenewo.

Ndimaganizanso kuti palibe munthu amene angakwanitse kundikopa ine pondifotokozera za kupezeka kwa mulengi ine mpaka kukhutira. Inali level imeneyi yolemara kazantshi kwa ine.

Nkhani imeneyo inali ikundidandaulitsa kazantshi.

Ndinayetsetsa kundi ndithane nazo ndikuyamba kuona zinthu zina.

Koma ndinali ndikuzifunsa ndekha kuti ndi njira yanji yomwa ndingatsatire pothana ndi zimenezi?!!!

Panjira ya chisangalalo choyaka ndi moyo waufupi, kapena panjira ina?!

Kunena zoona, chinthu chimenechi chinali nkhwawa yaikulu yondilemetsa ine usana ndi usiku.

Mpaka zinafika poti sindimakwanitsa kugona tulo.

Ndinali ndikutuluka mnyumba yanga kupita ku msika ku shop ya bambo anga ku msikako, ndipo zimayandikila kuti ndisadziwe munthu yemwe ali m'mbali mwanga chikisiwa cha nkhwawa ndi nkhwani imeneyi.

Zinafika poti amandigwira ena mwa azinzanga kundilonjera ine osawayankha chifukwa sindimawamva.

Mpaka amandigwira ndikumandifunsa kuti: ujeni kodi uli kuti?

Ndiye ndimazizimuka ndikukhala tcheru.

Kenako ndinatsimikiza kuti palibe kuchitira mwina koma ndikuyenera kuthana ndi chinthu chimenechi. Izi zichitike kudzera mu njira iyi kapena inayo.

Ndiye ndinayamba kuwerenga ma buku, ndicholinga choti ndifike kumapeto kwa nkhwani imeneyi. Ndipo ndisakubisileni, ndithudi ine ndinali ndikuwerenga ma buku akulu akulu koma palibe chomwe ndimapindulamo ngakhale liwu limodzi.

Ndinapitilira kukhala pa nyengo imeneyi kwa nthawi yaitali ine ndikuwerenga ma buku, ndimawerenga kalikonse komwe kagwa mmanja mwangamu.

Ndimafufuza ma umboni oti munthu ndikukhutisiwa za kupezeka kwa namalenga. Ndinakhala nthawi yaitali ndikutero.

Koma kuti Allah pamene anaona uchoonadi wanga za kulunjinga ku nkhwani imeneyi, ndithudi anandithandiza.

KUCHOKA KU CHIKAIKO KUPITA KU CHITSIMIKIZO

من الشك إلى اليقين

Nkhani yoona ya kufuna funa choonadi.

Chichewa — التشيشيو

Ndipo nditchula umboni umene unandilondolera ine kuchoka ku chikaiko kupita ku chitsimikizo, kukhulupilira mwa Allah.

Tsiku limeneli ndimalitcha kuti ndi Tsiku la chikhulupiliro.

Kena kalikonse kanasintha mu kaonedwe ndi mukaganizidwe kanga. Ndinayamba kuona tsopano za kupezeka kwa namalenga, kuona ndi kuganiza mwasapano. Ndiziyang'ana nkhope. Ndiye ndimazona kuti si nkhope zimene ndimazona dzulo zija ayi.

Ndimazona mitengo osati maonedwe amene ndimaionela m'mbuyomu.

Ndimaziyang'ana ndekha, ndi mwezi mayang'anidwe ena.

Ndinayamba kumuona Allah pa kena kalikonse, ndipo m'mbuyomu sindimamuona pa kalikonse.

Ayeretsedwe Allah.

Tsopano ndikupasani umboni oyamba omwe unandilondolera ine ku chikhulupiliro (imaan).

Zoona zake ndi zakuti, ndinali ndikuwerenga buku lotchedwa gharaibu al-makhluuqat (zodabwisa za zolengedwa).

Ndinali ndikuwerenga buku limeneli ndipo ndinapeza kuti pali mtundu wa Udzudzu.

Ukafuna kuti uchulukane mu nyengo yoswana, umaikila mazira mmitsinje ndi m madamu, umazifinya thupi lake, kudzera mtimabowo ta pathupi lake, timadzi timatuluka tomwe timauma mlenga lenga ngati tiulusi ta kangaude.

Umapanga tima bwato ting'ono ting'ono.

Choncho Udzudzu waukazi umapanga tima bwato ting'ono ting'ono ndikuikilamo timazira mu mtsinje. kenako mayi amafa. Kenakou timatuluka timphutsi ndipo timakula.

Timphutsi tija tikamakula timasanduka kekhalala Udzudzu ndipo munyengonso yobelekana umapanganso chimodzi modzi kuikila mazira kenako ndikufa.

Ndiye funso ndilakuti: ndi ndani anaika kachinthu kameneka kamene kamapangisa kuti kaziika ka bwato mthupi mwake?

Kachinthu kamene kamauma.

Ndi ndani amene anakaphunzitsa zopanga timphutsi?

Nanga ndi ndani amene anauphunzitsa kuti uzipanga kapangidwe ka mayi ake kumachita kuti mayi ake sanaone?

Mayi ake anafa, zikanakhala kuti unaona mayi ake tikanati unaphunzira kurohjera kwa mayi ake, ndiye ndi ndani anakaphunzitsa?

Chipanda nchitidwe umenewu ndiye kuti mtundu umenewu ukanaduka ndiye kuti Udzudzu ukanatha.

Izi zinaika kukhuzidwa kwakukulu mu mtima mwanga.

Ndi ndani anauphunzitsa Udzudzu kuti uzipanga zomwe mayi ake anapanga kumachita kuti siudaonane ndi mayi akewo?!!!

KUCHOKA KU CHIKAICO KUPITA KU CHITSIMIKIZO

من الشك إلى اليقين

Nkhani yoona ya kufuna funa choonadi.

Chichewa — التشيشوا

Chimodzi modzinso nkhani ina yofananilako ndi yomweyi imene anaifotokoza nzanga wa ine.

Iye anali ndi chida chomwe amasungilamo mazira, amaikamo m'menemo mazira a nkhuku.

Anaikamo m'menemo mazira 30 a nkhuku ndi zira lina limodzi la mbalame ya m'madzi lomwe anali nalo, anaika zira limeneli ndi cholinga choti lingokwanitsa chiwerengero cha nambala yosagawika ndi 2. Analika limodzi ndi mazira a nkhuku aja.

Ndiye nzanga uja anandiuza ine kuti: ine ndikudziwa tsiku limene mazirawa angaswe.

Akusimba kuti ndinabwera tsiku limeneli kudzayendera mazira aja kuti ndione ndi nthawi yanji imene ana angatuluke.

Akuti ndiye tinatuluka tiana ta nkhuku tokwana 30 kenako kanatuluka kamwana ka mbalame ya m'madzi limodzi ndi tinkhuku tija.

Nzanga uja anati: tiana tonse 30 ta nkhuku tija tinathamangila ku thengo, koma kamwana ka mbalame ya m'madzi kaja kanapita kokha mmadzi, kanayamba kusambila ndikuzisamala kokha kokha.

Inali mbalame ya m'madzi.

Zira lake linasweka limodzi ndi mazira a nkhuku.

Sikanaonepo mayi ake.

Ndichifukwa chani sikanatsatire tiana tinzake ta nkhuku tija ku thengo?

Ndi ndani anakauza ikoko kuti ndi mbalame ya m'madzi?

Kenako ndinaphunzira kuti njuchi zimapanga maselo a hexagonal.

Osanjidwa mwa dongosolo.

Ngakhale mutatenga dzira pa imodzi mwa izo n'kulisiya kwinakwake, dziralo limaswa n'kupanga maselo am'makona atatu. Amayikamo uchi.

Ngakhale sinaone mayi ake.

Zimenezi zinandikopa kwandvvi.

معهد السنة

الشيخ د. هيثم سرحان

sarhaan.com

mahadsunnah.com